Zimene Mungachite Kuti Banja Lanu Lizisangalala (Gawo 1)

Nkhaniyi yachokera m'buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* mutu 14. Bukuli likupezekanso pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso chifukwa chake mumazikhulupirira. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa kenako onani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI N'CHIYANI CHINGATHANDIZE KUTI BANJA LANU LIKHALE LOSANGALALA?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi anthu ena anganene zotani?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Malangizo ochokera kwa Mulungu angakuthandizeni kukhala ndi banja losangalala.
(Werengani mutu 14 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 1-4.)

Werengani Luka 11:28.
Mogwirizana ndi zimene Yesu ananena, kodi tiyenera kuchita chiyani kuti tizikhala osangalala?

Werengani Genesis 2:18, 21-24.
Kodi timadziwa bwanji kuti banja losangalala ndi mphatso yochokera kwa Mulungu?



Malangizo ochokera ku kampani yomwe inapanga chipangizo chinachake, amathandiza kuti muthe kulumikiza bwino chipangizocho. N'chimodzimodzinso ndi Baibulo, chifukwa choti linalembedwa ndi amene anayambitsa banja, limatithandiza kuti tikhale ndi banja losangalala

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Kuti mukhale ndi banja losangalala muyenera kuphunzira zimene Yesu ankachita.

(Werengani mutu 14 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 5-13.)

Werengani Aefeso 5:23, 25, 28, 29.

Ngakhale kuti Yesu sanakwatirepo, n'chifukwa chiyani ndi chitsanzo chabwino kwa amuna okwatira?

Werengani 1 Akorinto 11:3 ndi Aefeso 5:33b.

Yesu amagonjera Mulungu ngati mutu wake. Chifukwa chiyani Yesuyo ndi chitsanzo chabwino kwa akazi okwatiwa? (Werenganinso 1 Petulo 3:1-4.)

N'chifukwa chiyani inuyo mumakhulupirira kuti Mulungu amapereka malangizo abwino kwa anthu okwatirana?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

NGATI WINA WANENA KUTI…

Baibulo ndi buku lakalekale ndipo silingakhale ndi mfundo zothandiza mabanja a masiku ano.

MUNGAYANKHE KUTI…

Anthu ambiri angaterodi. Koma ndikukhulupirira kuti…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti?

_____

Poganizira zimene munthuyo wanena, kodi mungagwiritsire ntchito bwanji mfundo ya palembali kuti mumuthandize?

_____

NGATI WINA WANENA KUTI…

Zimene Baibulo limaphunzitsa zoti mwamuna ndi mutu wa banja zimapondereza akazi.

MUNGAYANKHE KUTI…

Anthu ena amaonadi choncho. Koma zimene Baibulo limaphunzitsa zimathandiza kuti tiziona akazi kukhala anthu ofunika kwambiri. Mwachitsanzo…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti?

_____

Poganizira zimene munthuyo wanena, kodi mungagwiritsire ntchito bwanji mfundo ya palembali kuti mumuthandize?

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania